ELECTRICITY SUPPLY CORPORATION OF MALAWI LIMITED (ESCOM)
KULUMIKIZA MPHAMVU YAMAGETSI PAKATI PA MAIKO A MOZAMBIQUE NDI MALAWI

NDONDOMEKO YA CHIPEPESO KWA ONSE OKHUDZIDWA NDI PULOJEKITIYI

CHIDZIWITSO KWA MAGULUPU, MAFUMU NDI ANTHU A MIDZI YONSE YOKHUDZIDWA M'MADERA AMENE NTHAMBO ZAMAGESTSI ZIDZADUTSE PA PULOJEKITIYI

KULENGEZA TSIKU LA 26 EPULO 2019, LIMENE LIRI LOMALIZA KUPANGA KALEMBERA WA MALO KAPENA KATUNDU AMENE ADZAKHUDZIDWE NDI PULOJEKITIYI

Kampani yazamagetsi ya ESCOM mothandizidwa ndi Boma la Malawi ikufuna kukoka mphamvu ya magetsi pogwiritsa nchito nthambo za 400 kV kuchokera ku Matambo (boma la Changara, mu chigawo cha Tete, m'dziko la Mozambique) kufika ku Phombeya (m'boma la Balaka, chigawo chakum'mwera, m'Malawi nmuno). Pulojekitiyi ikuyendetsedwa ndi chithandizo chochokera ku World Bank, Norwegian Trust Fund, KfW, European Union(EU) komanso Southern African Power Pool (SAPP).

Pulojekitiyi ndi mbali ya nchito yolumikiza mphamvu yamagetsi m'maiko a madera ena a mu Africa, ndi cholinga chotukula malonda a magetsi m'mayiko oyandikana ndi dziko la Malawi, ndinso kuonjezera kudalilika kwa mphamvu ndi nchito zamagetsi kuno ku Malawi. Ku Malawi kuno nthambo zamagetsi za mphamvu ya 400 kV imeneyi zidzakokedwa pa mtunda wokwana makilomita 76, kudutsa m'maboma a Mwanza kwa TA Kanduku ndi TA Nthache, Neno kwa TA Symon ndi TA Mlauli, ndi ku Balaka kwa Sub-TA Phalula, TA Nsamala. Pulojekitiyi idzakonzanso miseu yodutsamo pomanga nthambozi. Pulojekitiyi iri ndi dongosolo lotere:

- Mulifupi mwa njira yokoka nthambo (wayleave) mudzakhala mamita 55
- Utali wa mapolo kumwamba udzakhala osachepera mamita 44 koma osapitilira mamita 53
- Ntunda wa pakati pa mapolo udzakhala wautali mamita 450
- Tsinde la mapolo lidzakhala mamita 20 mulifupi ndi mamita 20 mulitali

Ichi ndi **chidziwitso** kwa anthu onse okhudzidwa (PAPs), magulupu ndi mafumu, kuti tsiku lomaliza kuyeza malo, nyumba ndi katundu amene adzakhudzidwe ndi Lachisanu pa **26 Epulo 2019.** Onse amene ali ndimafunso kapena nkhawa akudziwitsidwa kuti alankhule ndi anthu amene akuyang'anira nchito ya kalemeberayi kuyambira pa **6 Epulo kufikira pa 26th Epulo 2019.**

Chonde dziwani kuti **kuyabmbira pa 26 Epulo 2019**, sikoloredwa kumanga chirichonse mkati mwa malo amene adzakhazikitsidwe kuti ndi njira yomanga nthambo zamagetsizi. Aliyense amene adzamange chirichonse kapena kubzala mitengo patapita pa **26 Epulo 2019** sadzalandira chipepeso kuchokera ku pulojekitiyi. Ngati mufuna kdziwa zambiri lumikizanani ndi anthu awa:

Mr. Kent Kafatia, Water Waste and Environment Consultants: 0111 978 377 or 0888 831 595
Mr. Philippe Alary-Paquette, WSP Canada: +1 438 843 7791 or +1 514 616 9221
Mr. Precious Mpekansambo, Project Wayleave Specialist at ESCOM: 0991 555 661/0888619987